# Ndondomeko zothandiza kuunikira khalidwe loyenera kwa Anthu Ogwira Nchito za Chifundo

Anthu ogwira nchito za chifundo akhoza kulangidwa – **kapena kuchotsedwa nchito kumene** – **ngati atakhala ndi khalidwe loipa pa nkhani yogonana**.  Izi ndi ndondomeko zomwe ziyenera kutsatidwa ndi munthu aliyense ogwira ntchito za chifundo:

- Anthu ogwira nchito za Chifundo **saloledwa kukhala ndi chibwenzi ndi mwana wochepera zaka 18 zakubadwa, ngakhale malamulo a dziko lawo atawaloleza.** Kusadziwa  zaka zeni zeni za mwanayo sichifukwa chovemerezeka kuti munthu akhale pa chibwenzi ndi mwana wochepera zaka 18.

- Anthu ogwira nchito za Chifundo **saloledwa kugona ndi munthu yemwe akulandira chithandizo chomwe iwo akupereka, kapena kumulonjeza munthuyo kuti amupatsa ndalama, kumulemba ntchito, kapenaso kumupatsa katundu wochulukirapo**. Iwo sayeneranso kulonjeza munthuyo kuti adzamupatsa katundu ngati atavomera kuchita naye za chiwerewere. Izi ndizosaloledwa, kapenaso kugona ndi hule pomulipira ndalama.

- Anthu ogwira nchito za Chifundo amakhala ndi mphamvu yosankha omwe ayenera kulandira chithandizo monga katundu kapena zinchito zina. Pa chifukwa ichi, mabungwe a nchito za chifundo **amalimbikitsa anthu awo wonse wogwira nchito ya chifundo kuti asakhale ndi zibwenzi kapena kugonana ndi anthu omwe afunikira chithandizo kumalo awo**. Khalidwe la zibwenzili kapena logonana limapangitsa nchito yothandiza anthu kuti ioneke ngati yopanda chilungamo komanso yosadalilika.

- Ngati munthu ogwira nchito za Chifundo ali ndi **nkhawa kapena akuganizira** kuti wina wake mu bungwe limenelo kapena bungwe lina lopereka thandizo kwa anthu akuphwanya ndondomeko zoikidwazi, munthuyu **ayenera kuti aulule** zimenezo pogwiritsa nchito **ndondomeko** zoikidwa ndi bungwelo.

- Anthu ogwira nchito za Chifundo **ayenera kuonetsetsa** kuti malo ogwirako ntchito kusakhale mchitidwe woipa wa chiwerewere kapena zogonana. Anthuwa ayenera kulimbikitsa aliyense wogwira ntchito kuti **atsatire ndondomeko zoikidwazi** komanso akhale ndi khalidwe lovemerezeka malinga ndi malamulo omwe anaikidwa. **Mabwana onse** ali ndi udindo wowonetsetsa kuti pali malamulo oyenera komanso ndondomeko zokhazikika zokhudzana ndi nkhaniyi mu malo anchito.

Ngati mufuna kudziwa zambiri za IASC ndi mfundo zokhuza mkhalidwe woipa wogonana ndi nkhanza, zipezeka apa: http://www.pseataskforce.org/uploads/tools/sixcoreprinciplesrelatingtosea_iasc_english.doc.

Mfundo zimenezi zomveka mwatsatane-tsatane zinakhazikitsidwa mothandizana pakati pa mabungwe awiri – (IASC Task Team on Accountability to Affected Populations and Protection from Sexual Exploitation and Abuse and Translators without Borders.)